

CHICHEWA – “Who will deliver me?”


## NDANI ADZANDILANDITSA INE ?

Kale-kale tsiku la Mulungu ndidali kulalikirira Uthenga Wabwino pa mudzi wa mfumu ina m'dziko la Lesotho. Khamu lalikulu la anthu kuphatikizapo a mfumu ndi akazi awo anasonkhana kudzamva Mawu a Mulungu. Mawu a moyo amene ali a mphamvu ndi a kuthwa koposa lupanga lakuthwa konse-konse anapoyza kwakuya m'mitima ya anthuwo.

Ndikanali kulalikirabe, Mfumakanzi, mkazi wa mfumu yayikuluyo anayamba kulira kwambiri. Ndipo misozi ikutsikira m'masaya ake, Mfumakaziyo inaimirira ndikuyamba kulira mokweza: **Adzandilanditsa ndani? Ndapota nanu ndithandizeni, mtima wanga ukupweteka kwambiri; Ndini munthu wachisoni ndiwotayika. Angandithandize ndani? Adzandilanditsa ndani kunsinga zoopsyazi za imfa? Kalanga! Ndichitenji ine?** Nonsenu mukundidziwa kuti ndine Mfumakazi, mkazi wa Mfumu, komanso ndine m'modzi wa azimayi a chigwirizano.

Kwa zaka makumi awiri ndakhala ndikupitabe kutchalitchi, koma zonsezi sizidandithandize ndipo sizidandimasule kotero uchimo udandimangabe. Ndine woledzera, wambanda ndi wakupha. Manja anga aipitsidwa ndi kudetsedwa chifukwa ali ndi mphamvu zophikira mowa, chakumwa chotembereredwa chija. Uchimo wandimanga manja ndi miyendo ndipo ndiri m'kaidi wa ku Gehena Ili chikhalire Mfumakaziyo inalirabe koopsyazi ndi mofuula: **“Ndithandizeni! Ndithandizeni! Adzandilanditsa ndani? Adzandilanditsa ndani kumsinga**

### NDANI ADZANDILANDITSA INE ?



*“Iye wochita tchimo ali wochokera kwa mdierekezi. (1 Yohane 3:8)*

za uchimozi? Ndimamkonda Mulungu, koma uchimo ukuchita ulamuliro mwa ine ndi kundikokera ku Gehena. Ndinapha mwana wanga woyamba akadali wakhanda nditaledzera iye ali kumbuyo ndidaguduzika ndiphwanya mutu wa mwana wanga wokondekayo ndipo iye adafera pompo. Chonde ndithandizeni! Ndilanditseni ku imfayi. Chikunja sichidandithandize. Chipembedzo sichidandithandize. Angandithandize ndani? Adzandilanditsa ndani?”

**Ndidaiyankha kuti Mfumakaziyo: “Usaope ndipo usachite mantha. Vuto lako ndi vuto la munthu wina aliyense. Baibulo lomwe ndi mawu a Mulungu likupatsa yankho la kulira kwa mtima wako. Baibulo limati:”** Uchimo umalamulira miyoyo yathu koma pali m’modzi amene angatilanditse kunsinga zake.

Pakuti ndimadziwa kuti mwaine, kutanthauza thupi langa la uchimoli simungakhale chinthu chabwino, chifukwa ndimafuna kuchita zabwino, koma sindingathe kutero. Zabwino zimene ndikadachita, sindichita, koma choipa chimene ndidana nacho ndikusafuna kuchichita, ndicho chimene ndichichita. Uchimo umene uli mwa ine undiumiriza kosalekeza kuchita choipa ndipo chabwino chimene ndichifunitsitsa kuchichita sindichichita. Ndikondwerera m’chilamulo cha Yehova monga mwa munthu amene ali mkati mwanga; koma pali lamulo lina m’ziwalo zanga limene lichita nkondo ndi maganizo anga ndi chikumbumtima change ndikundibwezera mu ndende ya lamulo la uchimo. (Aroma 7:15-25). **Posachedwapa, kapena mtsogolo muno, kulira uku kudzifika mumtima wa aliyense: Kalanga ine! Munthu wopanda pache ine! Adzandilanditsa ndani ine?**

### **YAKHO LAKE**


***“Chifukwa chache ngati Mwana adzakuyesani inu a ufulu, mudzakhala mfulu ndithu.” (Yohane 8:36).***

Yesu Khirisitu ndiye yankho la mafunso athu onse ngakhalenso funso lako. Palibe chipulumutso mudzina lina liri lonse koma mu Dzina la Yesu Khirisitu (Machitidwe 4:12). Ndi dzina la Yesu Khirisitu yekha limene lingathe kutipulumutsa. Ndi mwazi wache wokha wokhetsedwa pamtanda umene ungate kutisambitsa ndi kutichotsera tchimo liri lonse. Palibe dotolo, mankhwala, sing’anga, munthu, mlaliki, wansembe, kapena tchalitchi limene linatipulumutse kutchimo. Ndi Yesu Khirisitu yekha, Mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene amachotsa machimo onse a dziko lapansi amene angathe kutipulumutsa ife ndi mwazi wake ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

Yesu Khirisitu, Mwana wa Mulungu anadza ku dziko la pansu kudzatsegula maso a anthu osaona. Kudzatulutsa am’ndende ndi iwo amene akhala mu mdima kuti atuluke mu mnyumba ya mndende (Yesaya 42:7). Ambuye Yesu anati: **“Aliyense wochita tchimo ali kapolo wa tchimolo ndi wa mdierekezi. Koma ngati Mwana wa Mulungu akuyesani afulu, mudzakhala mfulu ndithu.”** (Yohane 8:34-36). Yesu Khirisitu ndiye choonadi chimene chikhoza kutimasula.

**Yesu Khirisitu, Mwana wa Mulungu anatinyamulira machimo athu onse**

m'thupi lake pa mtanda paja. Machimo anthu onse anakhomedwa limodzi naye pamtanda. Zoonadi, lye ananyamula zowawa zathu ndi kusenza zisoni zathu. Koma lye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu. Chilango chotengera mtendere ife chinamgwera lye, ndipo ndi mikwingwirima yache ife tinachiritsidwa. (Yesaya 53:3-7).



*“Chifukwa chache ngati Mwana (YESU KHRISITU) adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu. (Yohane 8:36).*

**Baraba munthu wochimwitsitsa ndiponso wambanda ndi kupha anayenezedwa kufa**, kudzera mkupachikidwa, koma Yesu Khirisitu anatenga malo ake nanyamula mtanda umene Baraba akadaferapo. Yesu Khirisitu, Mwana wa Mulungu, anapachikidwa m'malo mwa Baraba, m'malo mwanu ndi m'malo mwanga. Baraba wambanda uja anamasulidwa chifukwa Yesu Khirisitu anamufera. Inu ndi ine tiri ngati Baraba uja ndipo **Yesu Khirisitu anatifera ife**.

Pakuti mphotho yache ya uchimo ndi imfa, koma mphatso ya Mulungu ndiwo moyo wosatha mwa Ambuye athu Yesu Khirisitu. Ngati muyang'ana ku mtanda wa Khirisitu ndi chikhulupiriro, mudzaona nokha kuti uchimo wanu utakhomedwa pa mtanda. Yesu Khirisitu anadzitengera malo anu pa mtanda kuti mukhale nawo moyo wosatha. Anakhetsa mwazi wache chifukwa cha chikhululukiro cha machimo anu. Pakuti Mulungu amakukondani kotero kuti anati patisa Mwana wache wobadwa yeskha kuti musaonongeke koma kuti mukhale nawo moyo wosatha.

Atamva mawu onsewa mkazi wa a Mfumu uja anayamba kukhulupirira kokwana mwa Yesu Khirisitu, napereka mtima wache kwa lye amene anamfera pa mtanda, nataya mwazi wache wamtengo wapatali kusambitsa machimo ache onse. Anapereka mtima wache woipa kwa Mulungu, ndipo Mulungu anampatsa

mtima watsopano namdzaza ndi Mzimu Woyera. Mulungu sadamkhululukire kokha, koma anamlanditsanso ku mphamvu ndi ulamuliro wa tchimo. Kwa zaka tsopano, mkazi wa mfumu ijayo akukhala moyo wabwino, wachipambano, wolakika ndi wangwiro. Ife samwanso mowa kapena kuchita china chiri chonse choledzeretsa. Iye sasutanso fodya wa ndudu kapena wam'mphuno koma akukhala moyo wabwino wosadetsedwa, ndipo ali mboni yolimbika ya choonadi kuti aliyense amene ali wa Yesu Khirisitu ali Wolengedwa watsopano: Zinthu za kale zapita, taonani, zakhala zatsopano (2 Akorinto 5:17).

Nawenso wowerengawe, ungather kumasulidwa mwa chikhulupiriro cha mwa Yesu Khirisitu, Ambuye wathu. Yesu anati: "Idzani kuno kwa Ine **NONSENU** akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu." Idza kwa Ambuye Yesu monga mmene uliri ndi kuli konse kumene uli. Muuzeni lye machimo ndi mavuto anu onse. Iye sadzakutayani mukadza kwa lye ndi mtima wodzichepetsa, wosweka ndi wokhulupirira. Mwinatu ungakhale wakale mum'pingo komabe ukadali womangidwabe mutchimo. Idza kwa Ambuye Yesu, ndipo lye adzakumasula nthwawi yomweyo, monga momwe muja anachiritsira wakhate ndi osaone uja. Ambuye Yesu ali yemwe uja amene akhoza kuchiritsa mtima wosweka ndi kumasula a m'ndende. Iye akhululukira mphulupulu zathu **ZONSE** nachiritsa nthenda zathu **ZONSE**. (Masalimo 103:3).

Ngati wapereka mtima wake **WONSE** kwa Ambuye Yesu, Mpulumutsi wathu, **AUZE** ena za lye amane **ANAKUPULUMUTSA**. Ifenso tidzakondwa kumvanso za inu mu m'kalata.

J,R. Gschwend

---

The popular "Heart Book" with its soul-saving message is obtainable in over 500 languages. Many have found salvation even just by looking at the pictures.

Kindly write to us if you are able to assist us with further translations of our free Gospel literature, informing us of the language into which you could translate this Gospel literature. Your assistance would be appreciated.

If you have found salvation in Christ, or have been otherwise blessed through our Gospel literature, please let us know. We would like to thank God with you, and remember you further in our prayers. **Our Heart of Man Book can now be downloaded in 480 different languages onto cell phones, tablets, etc from our website [www.angp-hb.co.za](http://www.angp-hb.co.za).**

For **free** Gospel literature, books and tracts in over 540 languages, write to:

**E-MAIL: [info@angp.co.za](mailto:info@angp.co.za)**

**ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS**  
**P.O. Box 2191, PRETORIA, 0001, R.S.A.**

(A Gospel Literature Mission financed by donations)

(Reg. No. 1961/001798/08)